EXAMINATION NO.: ______________________________

# SOUTH EAST EDUCATION DIVISION

**2024 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION MOCK EXAMINATION**

# CHICHEWA

**Subject Number: M032/II**

**Monday, 25th March** **Time Allowed: 2hours**

**1:00 – 3:00 pm**

## PAPER II

**(Malikisi 90)**

**MALANGIZO**

1. **Onetsetsani kuti pepalali lili ndi masamba osindikiza khumi ndi anayi.**
2. **M'gawo A:** Malamulo a Chiyankhulo: Yankhani mafunso onse. **(Malikisi 40)**.
3. **M'gawo B:** Kumvetsa nkhani: Yankhani mafunso onse. **(Malikisi 20)**.
4. **M'gawo C:** Chifupikitso. **(Malikisi 15)**
5. **M'gawo D:** Chimasulilo. **(Malikisi 15)**
6. Lembani **Dzina** lanu pamwamba pa tsamba **lililonse loyankhirapo.**
7. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

| Question Number | Tick if answered | Do not write in these columns | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 7 | | | |
| | | | |

©2024 SEED Turn over/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## Gawo A (Malikisi 40)

## MALAMULO ACHIYANKHULO

**Langizo: Yankhani mafunso onse m'gawo ili**

1. a. Tchulani mitundu ya agwirizanitsi omwe atsekedwa mzere kunsi kwao m'ziganizo zotsatira:

   (i) Anawa asazitenge ndalamazo.

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (ii) Mutu wanga ukundiwawa kwambiri

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (iii) Khasu limene mwatengalo si lathu

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (iv) Anyamata akhoza bwino mayeso

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (v) Mbuzi zanu zisanu zidasowa

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   b. Perekani ntchito za mifuwu yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

   (i) Ha! Inunso n'kukhala ndi mwana wophhunzira chonchi?

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (ii) Kalanga ine! Diresi langa latsopano lija lagwera pamoto

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

   (iii) Hehede! Mwana wanga wakhoza mayeso

   ______________________________ **(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(iv) Chete! Ndi nthawi yoti tiyambe mwambo wathu.

____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(vi) Mateyu chinya! Timwe tiyi wamkaka

____________________________________________ **(Malikisi 1)**

2. a. Pangani ziganizo ndi "ndi" poonetsa ntchito zotsatirazi

(i) Kukhala mneni wodalira

______________________________________________________________

____________________________________________________ **(Malikisi 2)**

Kukhala mlumikizi

______________________________________________________________

____________________________________________________ **(Malikisi 2)**

Kukhala mvekero

______________________________________________________________

____________________________________________________ **(Malikisi 2)**

b. Sinthani aneni omwe atsekedwa mzere m'ziganizo zotsatirazi kuti akhale mu msintho wa mneni wotsutsana:

(i) Tseka chitsekocho.

____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) Iwe yala pamthunzipo mkekawo.

____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) Ife timata kalatayi ngakhale atinene.

____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(iii) Sing'anga <u>watsirika</u> munda.

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

3. a. Perekani magulu a amimvekero yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

(i) Chibayo changoti <u>thi</u> mu nthiti mwangamu

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) Mateyu ali <u>zyoli</u> ngati nkhuku yadzoye

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) Yohane anangoti <u>bwereru</u> kunyumba kuthawa

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iv) Ophunzira anali <u>pikitipikiti</u> ku ofesi kwa a hedi

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(v) Zigawenga zidangoti <u>sololoku</u> kuchokera patchire

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

b. Perekani chachikazi cha mawu otsatirawa:

(i) Atatavyala

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) Kapolo

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) Muphwa

_____________________________________________________ **(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(iv) Tambala

__________________________________________________________ **(Malikisi 1)**

(vi) Ndoda

__________________________________________________________ **(Malikisi 1)**

4. a. Tchulani mitundu ndi ntchito ya akapandamneneni omwe ali ndi mzere kunsi kwao m'ziganizo zotsatirazi:

(i) Iye amakonda <u>nyama yowotcha.</u>

Mtundu:____________________________________________ **(Malikisi 1)**

Ntchito: ____________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii). Khazikani chakudyacho <u>pa tebulo lalikulu.</u>

<u>Mtundu: </u>____________________________________________ **(Malikisi 1)**

Ntchito:____________________________________________ **(Malikisi 1 )**

b. Sinthani ziganizo zotsatirazi kuti zikhale mu zoyankhula mwini.

(i) Iye adafuna kudziwa chomwe iwo adali kusema.

____________________________________________________________________

__________________________________________________________ **(Malikisi 2)**

(ii) Mtsogoleri wathu adatilangiza kuti tisamaononge zachilengedwe.

____________________________________________________________________

__________________________________________________________ **(Malikisi 2)**

(iii) Amayi adandiuza kuti ndizasamala ndi anthu abodza.

____________________________________________________________________

__________________________________________________________ **(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## GAWO B (MALIKISI 20)

5. **KUMVETSA NKHANI NDI KUSANTHULA CHIYANKHULO**

Werengani nkhani ili munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

‘Odi! Odi kuno!’ Adakuwa Salapu uku akugogoda pa chitseko ndi ndodo yake yoyendera. Padapita mphindi zingapo mwini wakeyo asadayankhe. Akusinkhsinkha zoti mwina anagogogoda pa zenera ndi pomwe adamva Ziligone akukhosomola ngati akuchotsa kachitsotso kukhosi.

‘Aa, kodi ndi a Salapa? Kwagwanji kuchita kundilawirira m’mawa chotere?’ adafunsa Ziligone uku akutsekula chitseko.

‘mzanga maganizo ndi omwe andivuta. Paja ukudziwa kuti alamu ako adachoka padzana paja titasemphana maganizo pankhani yokhuza uchembere wabwino. Ndakhala ndikuwayimbira tenifolo kuti abwerere kunyumba koma amenyetsa nkhwangwa pamwala kuti ngati sindisintha maganizo, mbambadi sadzapondanso pakhomo pathu,’ adafotokoza motero Salapa. Ziligone adamuyang’anitsitsa Salapa mochita kumutsitsa ndi kumukweza, kenaka adaseka chikhakhali. ‘Nanga ukuseka chiyani, bwanawe? Kodi amatero mnzako akakupeza ndi vuto? Addaandaula Salapa.

Mnzanga, apa sipafunika kukusereula ayi, mavuto enawa umachita kuwayamba dala. Kodi suja ndinakuuza kuti ana sachita kuberekera mangolomera. Tangoziyang’anira wekha: nsapato ulibe, buluku lidasintha mtundu kalekale chifukwa cha kusachapa, ndipo ana ako amachita kutsinana m’mbale kaamba ka kuchepa kwa chakudya. Ukuganiza kuti mkazi wako angabwerere zinthu zili chomwechi?’

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Salapa adalaswa mtima ndi mau olumaza bongo omwe adawamva kuchokera kwa munthu yemwe amayembekezera kuti ndi mnzake wapamtima ndipo amuthandiza. Mawu a Ziligone adawawa mu mtima mwake ngati tsabola wa piripiri. Mutu udachita chizungulire, magazi adatentha ndipo kwa kanthawi m'maganizo mwake mudalowa yeso longofuna atamujogoda Ziligone ndi ndodo yakeyo koma nkhongono zidamuchokera.

'Mzanga, ine sindidadukize tulo tanga ndi cholinga choti udzandithire moto wa mwano ayi. Ndimaganiza kuti uvomera kupita ku mudzi kwa a Malambo kuti ukamunyengerere mkazi wanga kuti abwerere, koma n'chachidziwikire kuti umangondikonda ndikamagula zipanda za mowa kwa a Nasimango basi.' Adayankhula motere Salapa, uku maso ali thwanithwani ndi ukali ngati galu womenyedwa ndi ndodo ya mbuye wake yemwe.

'Hehede! Vuto lako mnzanga ndi limenelo. Umangoganiza za perese basi. Koma ngati ukufuna mkazi wako abwere kunyumba, ndipo ukufuna kuti uziwombole mumsampha wa mavuto ako, chomwe ungachite ndi kuvomereza kuti uli pa mavuto chifukwa cha unkhutukumve wako. Taona momwe moyo wanga ndi wa apabanja anga udasinthira nditangosankha njira zamakono za kulera; ndili ndi ana omwe ndingathe kuwasamala, pakhomo panga ndi pa mwanaalirenji ndipo mkazi wanga adakawalabe ngati mtsikana wosatha msinkhu. Gwero la zonsezi ndi chisanzo chomwe tidapanga ngati banja kuti tiyambe kutsatira ndondmeko za uchemberee wabwino.

'Mmene Ziligone amakamba izi n'kuti Salapa akupumira m'mbali monga ng'ona yotopa nkufufuza madzi. . Adadzadzidwa ndi mkwiyo, koma mkwiyowo sudali wopita kwa mkazi wake kapena Ziligone koma iye mwini. Adazindikira kuti kwa nthawi yayitali adakhala akumva za njira zakulera monga jadere, lupu ndi jakisoni

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

zomwe adatsatira ndi kupindula koma nthawi zonse ankanyozera.

Tsiku lina Salapa adachita kumuonetsa mlangizi wa zauumoyo msana wa njira ya kwawo ati chifukwa adamuuza kuti padalinso njira ya kutseketsa kwa abambo. Silidali tsiku loyamba kuti amve za njirayi ayi. Kuchokera m'mapulogalamu osiyanasiyana omwe amaulitsidwa m'mawayilesi adali atamvapo za njirayi koma adatsimikiza mu mtima kuti nkhani za uchembere wabwino ndi njira zakulera zidali za amayi ndi abambo ochepa oduka mitu.

Salapa adaganaziranso momwe ana ake khumi ndi awiri amazunzikira ndi mavuto osiyanasiyana. Umphawi udachita ufumu pa khomo pake, ndipo adali mu ukonde wa njala yomwe idakhala ikumutsautsa zilumika zambiri. Ankalepheranso kugula zovala zoti mkazi ndi ana nkumatchena, chifukwa nthawi zambiri thumba lake limakhala lobooka.

'Apa mzanga ndiye wanditsekula m'maso. Ndikupita kwa a Malambo ndikamupemphe mkazi wanga kuti abwererenso. Ndikudziwa kuti chapita chapita dazi lilibe mankhwala komanso kuti ndichita ngati munthu wofika pa malo okwerera basi, basiyo itapita kale koma n'kofunika kuti ndichitepo kanthu basi. Ndikufuna ana anga amuna aphunzire kuti uchembere wabwino ukuyenera kuyamba ndi ife amuna.' Adatero Salapa, uku akuuyatsa ulendo wolunjika msewu wa kwa a Malambo.

**Tsopano yankhani mafunso atsatirawa**

a. (i) Kodi ndi chiyani chomwe chidachititsa kuti apite kunyumba kwa Ziligone?

______________________________________________________________

______________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(ii) Kodi mkazi wa Salapa kumudzi kwawo kudali kuti?

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) N'chiyani chomwe chidachititsa kuti mkazi wa Salapa achoke pakhomo pa Salapa?

___________________________________________________________

___________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

(iv) N'chifukwa chiyani Ziligone adamuseka Salapa atamuuza zamavuto ake?

___________________________________________________________

___________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

(v). Tchulani zinthu **ziwiri** zokha zomwe zikusowanyza kuti Ziligone adasankha chisankho chabwino potsatira ndondomeko za uchembere wabwino.

___________________________________________________________

___________________________________________________________

**(Malikisi 2)**

(vi) Kodi Salapa amatanthauzanji pamene amanena kuti adamuonetsa mlangizi wa zaumoyo msana wa njira yakwawo?

___________________________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

(vii) Tchulani mavuto **awiri okha** omwe Salapa ndi banja lake ankakumana mawo chifukwa chosatsata njira zakulera

___________________________________________________________

_______________________________________________ **(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

(viii) Kodi mkuluwiko woti "Chapita chapita dazi lilibe mankhwala" ukutanthauzanji m'nkhaniyi?

_______________________________________________

_______________________________________________ (**Malikisi 2)**

**b. Kusanthula chiyankhulo**

(i) Perekani matanthauzo a zining'a izi monga momwe zagwiritsidwira ntchito m'nkhaniyi.

1. Adagwira tambala pakamwa

   _______________________________________________ **(Malikisi 1)**

2. Amenyetsa nkhwangwa pamwala

   _______________________________________________ **(Malikisi 1)**

3. Wanditsekaula m'maso

   _______________________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii)Pezani mawu m'nkhaniyi omwe akufanana m'matanthauzo ndi mawu awa

(iii) Mphamvu

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

(iv) Akuganizaganiza

_______________________________________________ **(Malikisi 1)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## GAWO C (Malikisi 15)

### Chifupikitso

**6. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala. Ili ndi mawu 141 ndipo muifupikitse kuti ikhale ndi mawu osachepera 45 asapitirire 53**

MUNTHU WOLUMALA

Kulumala kulipo kosiyanasiyana. Pali anthu ena amene chibadwire chawo ndi olumala pamene ena amalumala atabadwa. Choncho tikhoza kuona kuti lungalunga mpobadwa chilema chichita kudza.

Munthu atha kulumala atachita ngozi ya galimoto, njinga, moto kapena kugwa mumtengo. Wolumala aliyense amakhala ndi vuto malingana ndi chiwalo chomwe iye adalumalacho. Ngati ndi olumala miyendo ndiye kuti kuyenda kumamuvuta motero sangathe kuyenda ngati munthu wina aliyense opanda chilema. Kulumala ndi chinthu chosautsa chifukwa munthu olumalayo amavutika pochita zinthu zimene zimakhala zapafupi kwa anthu opanda chilema.

Palibe munthu amene amachita kusankha kuti akhale wolumala. Kawirikawiri munthu amene adalumala manja amadalira anthu osalumala kuti amuthandize pochita zinthu zambiri monga kusamba ndi kudya.

Ndi chinthu chofunika komanso choyenera kuti wolumala azithandizidwa malingana ndi vuto limene ali nalo. Ndi chokondweretsa kuti mdziko lathu lino muli olumala ena amene ndi odzidalira pa zinthu zina zokhuza moyo wawo wa tsiku ndi tsiku.

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**GAWO D** (Malikisi 15)

**Chimasuliro**

7. **Masulirani nkhani yotsatirayi m'chichewa chomveka bwino.**

Child abuse is any form of maltreatment by an adult, which is violent or threatening for a child. It can also be neglect, which means lack of love, care and attention. Child abuse can be over a long period of time or just one-off action. It can happen in person or online.

Child abuse may cause physical and psychological problems. These problems can lead to anxiety, depression and substance use disorders. In order to hide the abuse from others, children may isolate themselves and have hard time making friends.

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for **FREE** from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**MAFUNSO ATHERA APA**

**NB: Pepalali lili ndi masamba otsindikiza khumi ndi anayi.**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com